

FORGIVING THE UNFORGIVABLE

Casper Ncube struggled with sexual immorality, drinking, smoking and fits of rage. But above all, he battled unforgiveness.

Casper grew up in a Christian family with parents who both claimed to be believers. Every Sunday, Casper attended church, looking pious on the outside but on the inside "I was not right nor did I have a personal relationship with Jesus Christ," he admits.

Casper was angry that his parents would speak about Christianity but never express love to him. "I couldn't understand them because the Light of God had not come to me," Casper recalls. "I would drink and smoke when no one was watching and I had a very short-temper."

During secondary school, Casper was popular and it gave him a sense of pride. "I [was so arrogant] I couldn't even allow someone to correct me," he admits. "One time, someone accidentally spilled salt onto my hand. I was very angry and took a hold of his collar and threatened to beat him."

Casper confesses that "I had a lot of unforgiveness in my heart that I didn't deal with and a lot of

anger because I grew up without anyone loving me."

Then, one day, he learned that his mother had been murdered. "I started hating that person and seeking revenge," he says.

However, Casper was tired of the evil, dark life that he was living. He knew there was a God, and he longed for something more.

He attended a Scripture Union Camp and the minister there preached a sermon that touched his heart and convicted him. During the altar call, Casper went forward.

"I accepted Christ and received Him into my heart," he says joyfully. "I prayed the sinners' prayer and I felt relieved and able to forgive. I had finally found someone to whom I could tell all my problems, someone who did not need my money but wanted me as I was."

It took time, but Casper, with

the Lord's help, was finally able to forgive his mother's murderer and let it go. "Now I have joy, peace and forgiveness in my heart!" Casper shares. "God gives me His love and His strength when I am feeling weak and makes me know how special I am to Him."

One of Casper's favourite Bible passages is Psalms 139:14 which says, "I will praise You, for I am fearfully and wonderfully made; marvellous are Your works, and that my soul knows very well".

To others who are struggling to feel loved and accepted, Casper shares these encouraging words, "God is not wanting you to first be righteous before coming to Him; He loves you as you are. There is a God in Heaven who loves us all unconditionally. He has a purpose for your life."

Casper is now studying for Christian ministry at the Back to the Bible Mission.

GOD LOVES YOU AS YOU ARE



Casper Ncube was able to forgive after he realised Jesus had forgiven him so much.

Kusangalatsa ana Page 5

BACK PAGE

SEASON OF SUCCESS

SYDNEY McLAUGHLIN

Kutayika kwakukulu koposa zonse

YOLEMEDWA NDI JOHN FINEGAN

KODI kufunika kwa chinthu chopezeka kwambiri ndi kotani? Anthu ndi ambiri padziko lino lapansi. Timapezeka paliponse. Kupezeka paliponse, kodi wina aliyense wa ife ndi ofunika?

Pakuona m'mene ambiri a ife timakhalira, tikhoza kunena kuti moyo wa munthu ndi ofunika pang'ono. Pamwamba pa zonse, timathamangira kupanga matupi athu kuti akhale bwino, koma osaganiza m'pang'ono pomwe za moyo wathu.

Yesu anafunsa mafunso abwino awiri: "Munthu adzapindulani akalandira dziko lonse, nataya moyo wake Kapena munthu adzapereka chiyani chifukwa cha moyo wake?" (Buku Lopatulika, Mateyu 16:26)

Chimene Yesu amafunsa chinali, "Kodi mukuganiza kuti moyo wanu ndi ofunika bwanji?" Kukhala munthu ndi kukhala ndi moyo ndi mzimu, munthu wosaonekayo, kukhala m'thupi looneka. Ndi gawo la uzimu limene limatipanga ifeyo chenicheni chimene tili.

Choncho moyo ukuyenera kukhala ofunika. Kodi Yesu amauona moyo kukhala ofunika kusiyana ndi m'mene ife timauonera? Ndipo ngati ndi choncho, n'chifukwa chiyani iye amaganiza kuti chuma chonse cha padziko lapansi si chokwanira ngakhale pa moyo umodzi? Ichi ndi

chimene chikuoneka kuti akuganiza pamene akufunsa mafunso amenewa.

Yankho likuyenera kupezeka pakuopsa kwa munthu "kutaya moyo wake."

Ndikhoza kuyang'anira thupi langa pakupewa zoopsa, pakudya chakudya chabwino, komanso pakugona malo abwino. Koma, tsiku lina thupi langa lidzafa. Sindingalepheretse izi kuchitika.

Koma nanga ndingauteteze bwanji komanso kusamalira moyo wanga?

Sindimauona, koma ndikudziwa ndilipo! Ameneyu ndi ineyo, amene ndili. Komanso, moyo wanga siudzasiya kukhala, chifukwa Mulungu anaupanga kuti udzakhale kwa muyaya. Ndiye ndingautaye bwanji?

Momveka bwino Yesu sakutanthauza kuti ndikhoza kutaya moyo wanga kuti ukhoza kufunika kuyang'anidwa kuti ndautaya penapake, kapena kuti ukungoyendayenda kwina kwake popanda ine!

Ayi, moyo wanga siungangotayika, koma ukhoza kumva kutayika, zimene Baibulo limanena kuti ndi "kuonongeka" Izi sizikugwirizana ndi thupi langa kufa ndi kukwiridwa. Koma ndi chimene chimachitika ndi moyo wanga ukachoka mu thupi langa likafa. Moyo wanga "kuonongeka"

sizikutanthauza kuti udzasiya kukhala tsiku lina. Koma "kuonongeka" kukutanthauza kuti moyo wanga siungabwezeretse kapena kuchira ku kutayika pamene ubwino onse umene Mulungu amapereka kwa ine nthawi imene ndili ndi moyo kwatengedwa kapena kuchotsedwa.

Ubwino umenewu ukufotokozeredwa mu Buku Lopatulika mochuluka. Mwachitsanzo mu Masalimo 145, ndime 9, timawerenga, "Ambuye

ndi wabwino kwa onse (anthu), ndipo chifundo chake chili pa zonse wazilenga"

Tonse ife, ndi dziko limene timakhalamo, timapindula kuchokera ku ubwino wa Mulungu tsiku ndi tsiku. Timasangalala ndi chakudya chimene dziko limameretsa kwa ife, usana, madzi, kutipatsa ife mphamvu ndi thanzi. Timasangalala kuthekera kwa kukonda ndi kukhala ndi maubale, kukhala ndi kumva bwino, timalankhula ndi kupanga dongosolo, timagwira ntchito ndi kuphunzira luso latsopano. Ubwino umachokera kwa Mulungu, koma tazolowera chisoni chimene kulakwitsa kwathu kumabweretsa m'miyoyo yathu, ndipo timalephera kuyamikira ubwino wa moyo umene umapatsidwa kwa ife.

KULIMBA KUPOSA UFITI



Richard Banda

“I ne ndinadwala, kutsala pang’ono kufa.”
 “Anandiuza kuti ayenera kung’amba thupi (opaleshoni) langa kuti akonze chiwalo, ndipo ndinadzazidwa ndi mantha a imfa,” akutero Richard Banda.

Iye sanadziwe kuti zichitika liti, koma ili linali tsiku limene Richard anasinthia zochitika za pa moyo wake m’mene anali m’chipatala.

Amalume ake amene ankamuphonzitsa Richard ufiti, anayesetsa kumuchiritsa iye, koma analephera, ndipo anamusiya mnyamata akupanga mantha ndi moyo wake.

Richard Rex Banda anabadwira m’banja lomwe linali la Chisilamu, koma losauka, ndipo anali ndi chiyembekezo chochepa cha ntchito, kenako iye anayamba kuba kuti athandizidwe ku zosowa zake, anayambanso kuba ngakhale kwa oyandikana nawo.

Iye anayamba kuphonzira ufiti kuti adzipindule nawo. “Kudzera mu ufiti, ndinapha anthu ambiri osalakwa,” iye anavomereza. “Si chifukwa chakuti iwo anandilakwira ine ayi, koma chifukwa chakuti sindinafuna kuti ndiwaone iwo

ali ndi moyo.” Izi ndi zinthu zoopisa kwambiri. Koma kuipa kunali kutsatira. “Mayi anga anamwalira m’chaka cha 1994. Ndipo ndikukhulupirira kuti panali anthu ena amene anawapha kudzera m’matsenga. Tsopano iwo anakwiya pobwezera, pakuti ndinapha anthu zosawerengeka.”

Pa tsiku limene amang’amba thupi langa, ndinamva wina wake akulalikira zokhudzana ndi Yesu Kristu. Izi zinandipangitsa kuti ndikhale ndi njala kuti ndiyambe kukhulupirira Iye. kenako ndi mtima wanga wonse ine ndinakhulupirira mwa Yesu, ndi kuti iye ndi amene angandichize ine.

Ndipo zikhulupiriro zonse zomwe ndinali nazo mu ufiti zinasandulika kukhala zachabe. Ndidziwa kuti zonse zomwe ndinkakhulupirira mu ufiti linali bodza, koma choonadi chimabisika mwa Yesu Kristu.”

Richard anapemphera kwa Mulungu. “Ine ndinamufunsa Yesu Kristu kuti alowe mtima mwanga, kuti andikhululukire zolakwa zanga zonse (machimo) ndi kuti

Iye alembe dzina langa m’Buku la Moyo (mbiri yangwiwo ya Mulungu yolembedwa yokhudza onse amene amamukhulupirira Iye.) Kulowa kwa Yesu mtima wanga kwasinthia moyo wanga kotheratu. Ntchito zanga zonse za kale sizilinsu mbali yanga ayi,” akutero Richard. “Mulungu wandipatsa mtima watsopano; womwe uli wodzadzana ndi chikondi cha pa Iye komanso odana ndi tchimo.

Sikuti ndi Richard yekha amene anasinthika monga m’mene akuperekeramba umboni, mbale wanga amene anandisiya ine chifukwa cha kusinthika kwanga kukhala Mkristu, ndipo tsopano ndi anzanga!”

Mau a Mulungu amatilangiza pa Levitiko 19:31, “Musamatembenukira kwa obwebweta, kapena anyanga; musawafuna, ndi kudetsedwa nawo; Ine ndine Yehova Mulungu wanu.”


“Chenjezo langa kwa iwo amene achita zosalongosoka m’moyo mwawo ndi machimo osiyanasiyana, ndikuti chonde ‘Lapani.’ Ngati mukumva kugogoda kwa Yesu m’mtima wanu, chonde mwachangu tsegulani khomo lanu kwa iye. Kunyozera iye, dziwani ichi, kuti chilango cha muyaya chikudikira inu. Lapani, satirani Kristu Yesu, Ambuyeyo,” Richard akutilangiza ife lero lino.

Timawerenga pa Aefeso 2:1-5 “Ndipo inu, anakupatsani moyo, pokhala munali akufa ndi zolakwa, ndi zochimwa zanu, zimene munayendamo kale, monga mwa mayendedwe a dziko lapansi lino, monga mwa mkulu wa ulamuliro wa mlengalenga (Satana), ... ndipo tinali ana a mkwiyo chibadwire, monganso otsalawo; koma Mulungu, wolemera chifundo, chifukwa cha chikondi chake chachikulu chimene anatikonda nacho, tingakhale tinali akufa m’zolakwa zathu, anapatsa moyo pamodzi ndi Kristu—muli opulumutsidwa ndi chisomo.”

ANAYAMBA KUPHUNZIRA UFITI KUTI ADZIPINDULE!

Coffee Break CROSSWORD & SUDOKU

- ACROSS**
- 1 Nail’s cousin!
 - 4 ___ and puffs
 - 7 Christ the Redeemer site
 - 8 Be achy and weak
 - 9 Perpendicular, vertical
 - 11 Australian bird
 - 12 Get it wrong
 - 14 Sea in Israel
 - 17 Thick pureed drink
 - 19 Long ___ (in the past)
 - 21 Cereal grain
 - 22 Tower of London birds
 - 25 A month (abb)
 - 26 A lyric poem
 - 27 French painter
 - 28 Ancient souvenir



- DOWN**
- 1 Plant support
 - 2 King or queen
 - 3 Metal beaten into shape
 - 4 A jump on one foot
 - 5 Winter bug
 - 6 Curved cavalry weapon
 - 10 Floral necklace
 - 13 Canyon feature
 - 15 Short stop in a journey
 - 16 Bird-to-be
 - 17 Play guitar strings
 - 18 Metal in rocks
 - 19 Coral-ring island
 - 20 Eye-linked
 - 23 Delivery vehicle
 - 24 Ropy sounding negative!

SOLUTIONS PAGE 7



“They squared the wagons. Are they allowed to do that?”

8				7			
	4			6			
1			9	5	2	4	
	5		1				
7		9			8		4
				8		2	
	1	3	2	4			7
				8			3
				1			6

Escaping prostitution

I was searching for someone to love me regardless of all my mistakes, Monica tells us. Rejected by her family and relatives because of her way of life, Monica was deeply regretting living a deceitful life.

She was born into a Christian church going family and knew the values of living that were taught. Sadly, she allowed herself to drift into a very different lifestyle. She had enjoyed her childhood with a good family relationship with parents who gave great care to their children. But says Monica, “I was not taking any heed of them.” Now trying to live with all the consequences of her mistakes, Monica felt very alone. “Nobody came to me to share the Word of God with me,” recalls Monica. However, in her loneliness she was not forgotten. There is a God who loved her regardless of the mess she had made of her life.

“Prostitution started to control my life and I could no longer hide it,” confesses Monica Khembo. “In front of my fellow Christians, I was like a saint, but I was not. I was a sly fox. Eventually, because of my rotten lifestyle, I was chased out of home by my parents. And because of this, I was influenced to enter an early marriage. I thought it would bring some rest; but things went contrary to that. In my marriage I had no peace. No one was happy with my behaviour, or my choices which I had ignorantly followed.”

One night she had a

vivid dream. In that dream, she recalls, “I was given a verse from Luke chapter 15 (in the Bible), and when I woke ... I read the verse, but I could not understand what God was really communicating.” Says Monica “I was much troubled in my spirit, and I had no peace at all.” Later, a pastor explained to her what was recorded in this chapter, spoken by Jesus Christ. “He told me that God really loves me and wants me to repent of my sin,” Monica tells us.

She was a very troubled woman, rejected by her parents and her relatives, suffering in her marriage, and feeling so very alone. But now she had heard that God loves her, regardless of her mistakes and was waiting for her to repent and look to him for forgiveness.

“I had nowhere to cast my burden other than to Jesus alone. This is how I came to be a Christian, (a Christ follower) explains Monica Khembo.

“I confessed my sin to Christ and allowed him to enter in my heart and then pleaded with him to pardon my sins, and to write my name and his Book of Life. I asked him to be my Lord and personal Saviour,” Monica tells us.

“God has completely changed my life since Jesus entered. I was completely lost but now I am found; he has changed my name from a prostitute to a pastor’s wife. I really thank God for that! Now I serve him and tell the world about the great love of Christ Jesus.” Monica now describes herself as, “a new creation, a child of God!”



Monica Khembo

If you would like to know more about God, systematic study of God’s Word (Bible), and grow spiritually, we welcome you to join a free Bible study course

Study the Bible with Emmaus Correspondence School

Over 70 years experience in correspondence ministry; nearly 25 million courses in 128 languages already distributed in more than 100 countries. Biblically sound & solid! Uncomplicated and straightforward. Flexible studying times – study at your own home, time & pace.


CONTACT:

Blantyre: ECS, PO BOX 31621, Chichiri, Blantyre 3

Zomba: ECS, PO BOX 768, Zomba

0885 010 009

0995 361 850
0888 004 853



230 Languages. 160 Countries. One Network. One Hope.

TRANS WORLD RADIO

Dedza	98.5 MHz	Mzuzu	106.3 MHz
Mchinji	96.7 MHz	Ntchisi	90.7 MHz
Lilongwe	106.3 MHz	Thyolo	101.8 MHz
Blantyre	90.6 MHz	Zomba	106.3 MHz
Dowa	93.9 MHz	Karonga	91.4 MHz
Mangochi	105.7 MHz		

Let them hear His voice

Psalm 29:1-11



Mantha a Imfa



Wilfred Kalolo

“Ndinalota maloto, ndipo m’maloto amenewo munthu wina ... anandiiza kuti sindimayenera kudzuka ndi moyo tsiku limenelo. Pamene ndinamva kuti ndimayenera kufa chifukwa cha uchimo wanga, ndinagwidwa ndi mantha. Ndinadandaula zokhudza moyo wanga wa uchimo. Ndinayamba kuganiza za m’mene ndinali komanso njira zanga zonse za uchimo.”

Umenewo unali m’ mawa wa Lamulungu—pa tsiku limene Wilfred Kalolo amakasinthidwa kwa muyaya.

Wilfred anakwatira, ali ndi ana ndipo amakhala kwa Chikanda mu boma la Zomba, Malawi. Akayang’ana m’mbuyo za moyo wake lisanafike Lamulungu limeneli iye akuti, “Ndinali wakufa m’ machimo anga.”

Iye akunena momasuka za moyo wonama, kuba, kuledzera ndi m’ mchitidwe wa chimasomaso.

Kukhala opanda Mulungu m’ moyo wake, Wilfred akuti anali wakufa m’ machimo ake, chifukwa amadziwa kuti analibe mphamvu zoletsera zoipa m’ moyo wake. Iye analibe chiyembekezo chilichonse cha kudzimasula yekha kukulakwa kwake kumene amakudziwa pamaso pa Mulungu amene amaona zonse.

Iye akupitiriza, “Mulungu amandikonda ndipo ndi wachifundo, pakuti sanandilole kuti ndife ndili mu uchimo m’ mawa umenewo. Iye wakhala akutumiza anthu kwa ine amene amandigawira uthenga wabwino wa Kristu. Koma moyo wanga umayendetsedwa ndi uchimo.”

Baibulo likufotokoza za bvuto limeneli! “Yesu anayankha kuti, “Zoonadi, Ine ndikuuzani kuti aliyense wochita tchimo ndi kapolo wa tchimolo.” Izi timawerenga mu Yohane 8:34, m’ Baibulo. Timachita zoipa chifukwa tili mu ukapolo wa uchimo.

“Ngakhale ndimaunyoza uthenga wabwino pamene umagawidwa kwa ine, Mulungu anapereka chisomo kwa anthu amenewa kuti asatope kundichitira umboni za Kristu, komanso kumandipempherera!”

Kuyang’ana m’mbuyo Wilfred tsopano akumvetsetsa kuti Mulungu amamufikira iye, kumuonetsera chisomo ndi kuleza mtima. Wilfred akuti, “Pomaliza iye anagwiritsa ntchito maloto, usiku uliwonse!” Patapita kanthawi Lamulungu limenelo ndinatsutsika

za uchimo wanga. Iye anapita kumene Akristu ena wotembenuka mtima amakumana. Kumeneko anauzidwanso za uthenga wabwino wakuti Yesu akhoza kukhululukira machimo ake chifukwa Yesu Kristu, wangwiro ndi munthu wopanda tchimo amene ndi Mwana wa Mulungu, anapereka moyo wake ngati nsembe kulipira uchimo wa Wilfred.

“Ndinapereka moyo wanga kwa Mulungu, kulapa machimo anga. Ndipo ndinapulumsidwa ku chilango cha uchimo wanga,” Wilfred akufotokoza. “Pa tsiku limenelo, ndinalandira Yesu Kristu monga Ambuye wanga komanso Mpulumutsi. Iye anandikhululukira ndi kuchotsa mphamvu ya uchimo m’ moyo wanga imene inandimanga mu ukapolo. Sindimaopanso imfa m’ mene ndimachitira ndisanapulumsidwe!

Ndimatumikira Ambuye pakuuza ena za umboni wanga, za m’ mene Yesu anasinthira moyo wanga komanso m’ mene ndinali opanda mphamvu kudzisinthana ndekha.”

“Anthu ena ankafuna nditasinthana pakundiiza mau a umunthu, koma zimenezo zinakanika,” akupitiriza, “koma Ambuye analowa mumtima mwanga ... iye wandisinthana kwa

muyaya!” Baibulo limatiuza ife, “N’ chifukwa chake, ngati munthu aliyense ali mwa Kristu, ndi wolengedwa kwatsopano; zinthu zakale zapita taonani, zakhala zatsopano. Zonsezi zichokera kwa kwa Mulungu amene anatiyanjanitsa ndi Iye mwini kudzera mwa Kristu ndipo anatipatsa ife utumiki wa chiyanjanitsa.” (2 Akorinto 5:17-18)

Chikhulupiriro cha Wilfred mwa Yesu Kristu chinakulitsidwa modabwitsa usiku wina wake. Iye anali ndi maloto oopsa amene anamuchititsadi mantha mpaka anaganiza kuti afa. Iye mothandizidwa ndi a Kristu ena wotembenuka mtima anapempherera pamodzi; ndipo kenako Wilfred anagona bwino bwino. Iwo anazindikira kuti mphamvu za kumtima za ufiti zimalimbana naye. Wilfred akuti, “Ambuye ananditeteza usiku umenewo.”

Iye akumaliza, “Tiyeni tithawire kwa Yesu kuti miyoyo yathu ipulumuke, iye adzachotsa mantha a imfa ndipo adzatiteteza ku mphamvu za mdima.”

Tiyeni Baibulo likhale ndi mau omaliza, pakuti timawerenga mu Yohane, mutu 3 ndime 16-18, “Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi, koteru anapereka Mwana wake wobadwa yekha, kuti aliyense wokhulupirira Iye asatayike koma akhale ndi moyo wosatha. Pakuti Mulungu sanatume Mwana wake ku dziko lapansi, kuti akaweruze, koma kuti akapululumutse dziko lapansi. Aliyense wokhulupirira Iye saweruzidwa, koma aliyense wosakhulupirira waweruzidwa kale chifukwa sanakhulupirire dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu.”

UCHIMO UMAVULAZA!

Kukhala ku Zomba monga mu mayi wachichepere amene ali ndi ana awiri koma osakhala pa banja si moyo wophweka. Koma Cecelia John ali ndi kochokera thandizo lake ndi chitetezo tsiku ndi tsiku kodabwitsa. Zinthu sizimakhala chonchi nthawi zonse.

“Ndimakhala moyo womvetsa chisoni komanso wopanda chiyembekezo. Ndinali wa chimasomaso komanso wakuba,” akutero Cecelia, “ndipo kupatula zimenezi, ndimadzitchula ndekha kuti ndine Mkristu komanso anthu ena amandionanso choncho. Ndimatha kupita ku tchalitchi, ndimayimba ndi kuchita zina zonse za chipembezo zimene Akristu amachita.”

Kukhala moyo wosakaniza ngati uyu umamubweretsera Cecelia mavuto. Kupangitsa moyo wake kukhala ovuta kwambiri, iye amavutikanso kulera ana ake awiri pa iye yekha.

Iye samadziwa za kusintha kumene Mulungu amafuna kumuonetsa—chifukwa amamukonzera zinthu zazikulu pa moyo wake.

Akristu ena oonadi anakhazikitsa utumiki ku Zomba opereka ngongole zopanda chiongola dzanja kapena kuti interest cholinga chothandiza anthu, amene ena anali ngati Cecelia, kuti adziyambira malonda ang’ onong’ ono kuti akhale odziimira pawokha pa nkhani ya zachuma.

Iye akuti uza ife, “Tsiku lina ndinasonkhana ndi gulu la amayi anzanga pa nkhani za ngongole zopanda chiongola dzanja zimenezi. Mulungu anayamba kundionetsa m’ mene ndinalidi ochimwa. Mulungu sanasiye kundilankhula ine ndipo ananditsutsa za uchimo wanga, kudzera mu ulaliki ndi Mau a Mulungu, Baibulo. Ndinayamba kuganiza zokhudza moyo wanga, kuti ngati ndingamwalire, kodi ndikakhala kuti, komanso kuti Mulungu amandiona bwanji m’ mene ndili mu uchimo wanga?”

“Kenako ndinagwiridwa ndi mantha a imfa, ndipo ndinafunitsitsa kulapa ndi kukhulupirira Yesu pa chipulumutso (kumachimo anga).”

Patapita masiku ochepa iye anakakhala nawonso pa gulu limeneli lobwerekera ndalama popanda chiongola dzanja ndipo anamva mau awa ochokera mu Baibulo: “Thawani dama. Machimo onse amene munthu amachita amakhala kunja kwa thupi lake, koma amene amachita machimo okhudza chigololo, amachimwira thupi lake lomwe. Kodi simukudziwa kuti thupi lanu ndi Nyumba ya Mzimu Woyera, amene ali mwa inu, amene mwalandira kuchokera kwa Mulungu? Inu simuli panokha ayi. Ndinu ochita kugulidwa. N’ chifukwa chake Lemekezani Mulungu m’ thupi lanu.” (I Akorinto 6:18-20)

“Ndinatsimikizika,” akupitiriza, “palibe uchimo umene Mulungu sangakhululuke ngati nditalapadi, kudzera mwa Yesu Kristu chifukwa cha imfa yake pa moyo wanga, komanso kuuka kwake kwa akufa.”

Ndinayamba kudziwana ndekha komanso chilichonse chimene ndinachita chili poyera pamaso pake.”

Baibulo limatiuza ife, “Pakuti Mau a Mulungu ali amoyo, ndi ochitachita, ndi akuthwa koposa lupanga lakuthwa konse konse, napyozza kufikira kugawira moyo ndi mzimu, ndi zifundo ndi mafuta a m’ mafupa, nazindikiritsa zolingirira ndi zitsimikizo za mtima.

“Ndipo palibe cholembedwa chosaonekera pamaso pake, koma



Cecelia John

zonse zikhala za pambalambanda ndi zobvundukuka pamaso pake pa Iye amene tichita naye.” (Aheberi 4:12-13).

Cecelia anakhulupirira Yesu Kristu kuti amukhululukire ndi kumusintha. Iye akuti, “Ndinamupempha kuti aphe zilakolako zanga zogonana, kundithandiza kuti ndisamabe, kundipatsa mtima wachifundo, ndi kunditsuka maganizo anga onyasa, ndi kuchotsa chilichonse m’ moyo wanga chimene chinali chosamusangalatsa iye (Yesu).”

Iye akupitiriza, “Ndikuthokoza Mulungu pakundipulumutsa—popanda kulipira kapena kuchita chinachake chabwino (kuti Mulungu andikonde). Ndili woyamikanso pakundichotsa ku mdima (wa uchimo) ndi pakundibweretsa mu kuunika kwake kodabwitsa.”

“Mulungu anasinthana zilakolako zanga. Zoganiza zanga zonse ndi zochita zakale zonse zinapita! Ndili ndi kopita ndi koyika zolemetsa ndi madandaulo anga! Ndipo chifukwa Kristu anandipulumutsa ku machimo anga palibenso chimene chingamubvute kuchita.

Cecelia wakhala akusonkhana ndi enanso amene miyoyo yawo inapulumsidwanso ku miyoyo yawo ya uchimo. Iwonso akukhala m’ moyo wobweretsa ulemberero ku dzina la Yesu, kuphunzira kumvera Mau ake ndi kudalira iye kuwatsogolera m’ madera onse a moyo.

“Pamene ndinali osapulumsidwa ku uchimo wanga, ndimadalira pa nzeru zanga, koma tsopano ndimadalira pa Mau ake. Mulungu ndiye nzeru zanga, mphamvu zanga pamene ndafooka.

“Sindineno kapolo wa uchimo, pakuti iye anandinyamulira zolakwa zanga pa iye pamtanda—pamene anandifera kuti ndikhale mfulu, monga ananena mu Yohane 8:36 ‘N’ chifukwa chake ngati Mwana adzakumasulani, mudzakhala mfulu ndithu.”

“Tsopano ndili ndi moyo wosatha, chiyembekezo chosatha, komanso moyo wamuyaya ndi Kristu Mbuye wanga komanso Mpulumutsi wanga.”

M’ Baibulo ophunzira Yohane anafotokoza m’ mene zimakhallira kukhala m’ moyo ndi Yesu mu imodzi mwa makalata ake, imene timaidziwa ngati Yohane Woyamba, mu mutu 5 ndime 13 timawerenga, “Ine ndikulemba zimenezi kwa inu, amene mwakhulupirira dzina la Mwana wa Mulungu kuti mudziwe kuti muli ndi moyo wosatha.”

Kodi inu muli wokhululukidwanso komanso pa mtendere ndi Mulungu? Kodi mukudziwadi motsimikiza kuti muli ndi moyo wake mwa inu?

Ngati mulibe chitsimikizo, funani Mulungu ndi chipulumutso chake.



But God demonstrates his own love for us in this: While we were still sinners, Christ died for us. - ROMANS 5:8 NIV

Kugwera mu 'khola la nkhumba'



YOLEMBEDWA NDI JODY BENNETT

Nkhani ya moyo wa Scott Harrison ikumveka pang'ono ngati ya mwana wolowerera. Iye anakulira mu banja la Chikristu ku mzinda ndi makolo amene amamukonda, komanso amayimba piano ku tchalitchi, koma anakhala zaka khumi za thunthu za moyo wake mosiyana ndi m'mene anakulira. Ali ndi zaka 18 anapita ku New York kumene anakayamba gulu loyimba. Pamene gulu loyimbali linatha iye anakhala wolimbikitsa za kuchitikachitika za ku tavern—analipiridwa kuti adzamwa mowa komanso kuchita za uhule.

“Aliyense ndinamupatsa chala kenako ndinapita kukagona, uvu ndi mwambi wa mahule. Ndimasuta mapukusi awiri a fodya pa tsiku, ndipo ndimakhala woledzera pafupifupi usiku wina uliwonse, kuchita juga ndi kugwiritsa ntchito mankhwala ozunguza bongo kupatula heroine,” Scott anauza msonkhano wa Veritas mu chaka cha 2017.

“Kumapeto kwake ndinakapezeka mu 'khola la nkhumba.' Osati kuti kukhala wosowa koma kuzindikira kunyansa kumene ndinaupanga moyo wanga. Ndimadzida ndekha. Sindine wachilungamo. Ndimagwiritsa ntchito mankhwala ozunguza ubongo m'banda kucha.”

“Ndinadzimva kunyansa, wosadzisamalira ndi wochititsidwa manyazi. Ndimangotha pa kungodziganizira kokha. Ndinazindikira kuti sindidzakhutitsidwa. Sindidzakhutitsidwa ndi akazi, sindidzakhutitsidwa ndi ndalama, komanso sindidzakhutitsidwa ndi mapwando.”

“Moyo wanga wa uzimu unali opanda kanthu. Kamvetsedwe kanga kanali kopanda kanthu. Ndipo chikhalidwe changa chinalinso chopanda kanthu,” iye akuvomereza pa kanema wa YouTube okhudza bungwe lake la chifundo.

Mu nthawi imeneyi, makolo ake a Scott anali akumupempherera mosalekeza. Kenako anawerenga buku limene bambo ake anamutumizira lotchedwa In Pursuit of God (Pakumufuna Mulungu) lolembedwa ndi A.W. Tozer, Mu buku limeneli Scott anaona zinthu zosiyana kwambiri

ndi moyo wake – chiyero, kuchita ndi kunena zolondola, chikhalidwe, umulungu, kusadetsedwa – ndipo anazindikira kuti zimenezi ndi zimene iye amafuna.

“Tsopano ndinayamba kumva kutsutsika chifukwa chokhala ndi chibwenzi changa, kugwiritsa ntchito mankhwala ozunguza ubongo komanso kuledzeretsa anthu kuti ndidzapeze ndalama,” akuvomereza. Kwa miyezi isanu kapena isanu ndi umodzi analimbana ndi kutsutsika ndi kulakwa kwake ndipo kenako anaganiza kuti basi kwakwana ndi kusiya moyo wake wakale pa kukwera galimoto lake ndi kuchoka.

Iye anapanga chiganizo chokhala moyo chifukwa anthu ena osati mwa iye yekha, atawerenga mu Baibulo buku la Yakobo (pa mutu 1, ndime 27) “Chipembedzo chimene Mulungu Atate athu amachivomereza kuti ndi changwiro ndi chopanda zolakwika ndi ichi: kusamalira ana amasiye ndi akazi amasiye pa mavuto awo, ndi kudzisunga bwino kuopa kudetsedwa ndi dziko lapansi.”

Atagulitsa pafupifupi chilichonse chimene anali nacho, kudera la Moosehead Lake, Maine pa internet café analemba mapepala kupereka moyo wake kwa chaka kuti akatumikire ku bungwe loona zothandiza anthu.

Zokhudza zochita zake zoononga, Scott anaganiza kuti njira yabwino ndi kusiyiratu zonse, pakamodzi. Iye anadziwa kuti chimenecho ndiye chabwino kwa iye, choncho anasiya kumwa mowa, mankhwala ozunguza ubongo, zolaula ndi kusuta.

Poyamba, chifukwa cha kale lake, panalibe bungwe limene linafuna kumutenga Scott. Kumapeto kwake a Mercy Ships anavomera kuti akhoza kudzipereka ku ntchito yawo ngati angawalipire iwo ndalama yokwana \$500 pa mwezi chifukwa chomupatsa mpata umenewu, zimene iye anapanga mokondwera! Iye anakhala nawo pamodzi ndi sitima ya chipatala imene idzapita ku Liberia.

Scott anapezeka kuti akutumikira ndi “madokotala a Chikristu amene amaonetsera chikhulupiriro chawo mu njira yeniyeni.” Monga Dokotala Gary Parker, amene anali atasiya ntchito yake yopanga ma plastic surgery ku California ndi

cholinga chakuti adzakachotsa zotupa ndi kukonza milomo yobadwa ndi chilema kwa anthu osaukitsitsa.

Pamene amatumikira ngati mtolankhani wotenga zithunzi wa Mercy Ships, kulemba za kusintha kumene amabweretsa kwa odwala komanso olumala m'madera osaukitsitsa ku Africa, Scott anakhudzika ndi kuchuluka kwa chiwerengero cha anthu amene samawatha kuwathandiza chifukwa cha kuperewera kwa zipangizo. Ulendo wina mpaka anabweza anthu zikwi zikwi, ena mwa iwo amene anali atayenda kwa mwezi kuti adzapeze chithandizo cha a chipatala

Kupita m'midzi ndi madera Scott anazindikira kuti matenda ambiri amene anthu amenewa amadwala anali chifukwa cha madzi osakhala bwino amene amamwa. Iwo amadalira madzi a umve ochokera m'zidekwe ndi m'mitsinje amene anali odzadza ndi ndowe za nyama komanso tizirombo.

Scott anaganiza zothana ndi bvutoli pamene linayambira pakupeza ndalama zokakumbira zitsime za madzi. Ndiye kuti izi sizimakathandiza anthu kuti angopeza madzi abwino okha, koma azimayi kuti adzathe kugwira ntchito ndi atsikana kumapita ku sukulu kusiyana ndi kumayenda mtunda wautali pafupifupi tsiku lonse kukapeza madzi, amene amakawatenga m'zigubu zolemera pamitu pawo.

Ndiye choncho bungwe Charity Water (Madzi a Chifundo) linapangidwa.

Monga munthu amene kale amalimbikitsa za zisangalalo za usiku, Scott anayamba zonse ndi phwando. Pa tsiku lokumbukira kuti wakwanitsa zaka 31 zakubadwa iye anapangitsa chochitika chachikulu ndi kumalipiritsa aliyense ndalama yokwana \$20 pakhomo. M'malo moti atenge ndalama zokwana \$1500, iye anazigwiritsa ntchito pakumanga zitsime zitatu ndi kukonzetsa zinzano zitatu ku malo osungira anthu othawa nkondo ku mphotho kwa dziko la Uganda. Ndipo kenako iye anatumiza zithunzi, komanso njira ya makono yodziwira ku

malo pogwiritsa ntchito makina a internet ya GPS, ndi nkhanayi kwa anthu 700 kukawaonetsa m'mene ndalama zawo zinagwirira ntchito.

Chifukwa anthu ambiri samakhulupirira mabungwe a chifundo, Scott anaganiza zochita zinthu mosiyana, kutsimikizira kuti ndalama zonse zoperekedwa zipita kukagwiritsidwa ntchito ku madzi a ukhondo pakupanga

thumba lapadera loyendetsera ntchito. Iye anatsimikiziranso za ntchito, kuika zolumikizira GPS ndi zithunzi pa Google maps, cholinga anthu athe kudziwa

kumene ndalama zinapita.

Zipangizo zothandizira kuzindikiritsa zinaikidwa pa mijigo, kuti anthu adzatha kutsata kuti ndi madzi ochuluka bwanji amene akutulutsidwa. Iwo anagwiritsa ntchito anthu a ku maderako kuti ntchito yekha yokhazikika ndi kupitirira.

Ndi zoonetsera ku gulu kwa anthu, ndawala zoyenda zokhudza madzi ndi zolengeza mwa luso anakweza kufunikira kwa madzi a ukhondo ndipo anthu anayamba kumeta ndevu,

kukwera mapiri komanso kupereka kukumbukira masiku akubadwa kwawo ndi cholinga chopeza ndalama za zitsime.

Monga Rachel Beckwith, amene anapeza ndalama zokwana \$220 pa tsiku lokumbukira kubadwa kwake pamene amakwanitsa zaka 9. Iye anali wokhumudwa kuti sanafikire pa mlingo umene ankafuna kufikitsa wa \$300 koma

pamene anaphedwa pa ngozi ya galimoto asanapangenso chisangalalo china chokumbukira kuti wakwanitsa zaka 10 zakubadwa, ntchito yake yopeza ndalama inafalikira koposa ndipo inapeza ndalama zoopsa \$1.2 million dollars ya madzi a

ukhondo!

